



ZOCHITIKA KUMAPETO A DZIKO LAPANSI



"Gula choonadi ndipo usachigilitse;
ugulenso nzeru, mwambo ndiponso
kumvetsa zinthu bwino." (Miyambo
23:23.CCL)

Kulalikidwa kwa Uthenga Wabwino padziko lonse lapansi ndiko kudzakhale chimake chosonyeza mapeto a mbiri yake (Mateyu 24:14).

Kulalikira kumeneku kudzatsogoleredwa ndi kutsanulidwa kwa Mzimu Woyeru, ndi mphamvu yofanana ndi yomwe inatsika pa tsiku la Pentekoste. Chochitika ichi chimadziwika kuti “mvula yamasika”.

Ndi ndani amene adzalandire mvula ya masika? Iwo amene asankha kukhala okhulupirika kwa Mulungu, kumvera malamulo ake, ndi kumutamanda moyenerera. Amenewa adzaikidwa “chizindikiro cha Mulungu wamoyo” (Chivumbulutso 7:2).



Kukonzekera msautso womaliza :



Kutsogoleredwa ndi Mawu.



Kusindikizidwa pamphumi.



Wokhulupirika pa kulambira.



Mphamvu yochokera kumwamba:



Mvula yamasika.



Kulalikidwa kwa Uthenga Wabwino.






KUKONZEKERA MSAUTSO WOMALIZA

KUTSOGOZEDWA NDI MAWU

“Mau anu ndiwo nyali ya ku mapazi anga, ndi kuunika kwa panjira panga” (Masalimo 119:105)

Kodi mumakudziwa kumene mungapeze choonadi chonena za kutha kwa dziko? Njira yake ndi iyi:

“Gula choonadi ndipo usachigulitse” (Miyambo 23:23)



“Ndipo mudzazindikira choonadi” (Yohane 8:32)

“Mau anu ndi choonadi”
(John 17:17)

“Mawu anu akamaphunzitsidwa amapereka
kuwunika; ngakhale anthu wamba amamvetsetsa”
(Masalimo 119:130)

Nthawi yakumapeto Satana adzaloledwa kuchita zozizwitsa zenizeni
ndi kubweretsa chinyengo chochenjeretsa kudzakhala kovuta
kwambirikuti kutsutsa (Chivumbulutso 13:13-14; Mateyu 24:24).

Kudziwa bwino Baibulo kokha, mothandizidwa ndi Mzimu Woyera,
kudzatithandiza kukhalabe olimba pa choonadi (2 Petro 1:19-21).




KUSINDIKIZIDWA PAMPHUMI

"Ndipo ndinapenya, taonani, Mwanawankhosayo alikuimirira pa phiri la Ziyoni, ndipo pamodzi ndi Iye zikwi zana mphambu makumi anai kudza anai, akukhala nalo dzina lake ndi dzina la Atate wake lolembedwa pamphumi pao" (Chivumbulutso 14:1)


Chizindikiro cha Mulungu chimazindikirika mu njira zitatu zosiyana :

- 1. Mzimu Woyer. Okhulupirira a mibadwo yonse amasindikizidwa ndi iye (Aefeso 4:30).**
- 2. Dzina, kapena khalidwe la Mulungu. Onse amene apambana adzalirandira (Chivumbulutso 14:1; 22:4).**
- 3. Chizindikiro chodziwika (Chivumbulutso 9:4; Ezikeli 9:4).**

Mulungu anasiya chisindikizo chake pa limodzi la malamulo khumi, monga chizindikiro cha anthu amene amamulambira(Ezikieli 20:20).



Zigawo za chisindikizo	Chitsanzo: ndalamaya euro (Spain)	Sabata (Eksodo 20:8-11)
Dzina	Philip VI	Yehova
Chiyenerezo	Mfumu	Mlengi
Dziko	Spain	Miyamba, nthaka ndi nyanja



KUSINDIKIZIDWA PAMPHUMI

"Ndipo ndinapenya, taonani, Mwanawankhosayo alikuimirira pa phiri la Ziyoni, ndipo pamodzi ndi Iye zikwi zana mphambu makumi anai kudza anai, akukhala nalo dzina lake ndi dzina la Atate wake lolembedwa pamphumi pao"
(Chivumbulutso 14:1)



Chizindikiroch, chitha kulandiridwa mu njira ziwiri: pamphumi kapena padzanja. Pamene okhulupirira adzachilandira pamphumi pao, osakhulupirira adzachilandira pamphumi pao kapena padzanja pao (Chivumbulutso 13:16). Kodi zikusiyana motani?



Ngakhale kuti Satana sasamala zifukwa zolambirira, Mulungu amavomereza kulambira koona mtima ndi kotheratu kokha (Aroma 12:1).

WOKHULUPIRIKA PA KULAMBIRA

"ndi kuti munthu sangakhoze kugula kapena kugulitsa, koma iye yekha wakukhala nacho chilembo, ndilo dzina la chirombo, kapena chiwerengero cha dzina lake" (Chivumbulutso 13:17)

Iwo amene akana kulandira chizindikiro cha chirombo sangagule kapena kugulitsa, ndipo akuwopsezewa ndi imfa (Chivumbulutso 13:15-17). Mbali inayi, ngati alandira chizindikiro, adzavutika ndi miliri yotsiriza ndi "imfa yachiwiri", kutaya moyo wosatha. (Chivumbulutso 16:2 ; 14:9-11; 20:4, 13-15).



Koma kodi chizindikiro cha chilombo n'chiyani? Chip, barcode, zinthu zowongolera thupi?



Ngati Sabata liri chizindikiro chowoneka cha okhulupirika, kodi chizindikiro cha chirombo sichikuyenera kukhala ndi makhaldwe ofanana?

Popeza kuti Baibulo silinena za kusintha kulikonse kwa tsiku lopembedza, Kusonyeza kuti kuvomereza Tsiku loyamba lapamulungu ngati tsiku la kulambira, ndiko kuvomereza ulamuliro wa Mpingo umene unasintha tsikuli (wotchedwa 666).



Ndi tidzalandira ulamuliro wotani? Ulamuliro wa bungwe la anthu kapena ulamuliro wa Mulungu, owonekera bwino lomwe mu mawu ake?



MPHAMVU YOCHOKERA KUMWAMBA

MVULA YAMASIKA



“Mukondwere tsono, inu ana a Ziyoni, nimusekerere m’Yehova Mulungu wanu; pakuti adzayamba kukupatsani mvula ya chizimalupsa, monga mwa chilungamo chake; nakuvumbitsirani mvula, mvula ya chizimalupsa ndi ya masika mwezi woyamba” (Yoweli 2:23).

Mneneri Yoweli amagwiritsa ntchito mvula monga fanizo la kutsanulidwa kwa Mzimu Woyeria (Yoweli 2:23, 28). Umunso ndi m’mene Petro anazigwiritsira ntchito mukulankhula kwake pa tsiku la Pentekoste (Machitidwe 2:14-17).

“Mvula” imeneyi imabweretsa chidziŵitso chonena za Mulungu (Hoseya 6:3). Munthawi yake, adatembenuza zikwizikwi tsiku limodzi (Machitidwe 2:41).

Nyengo ya ku Mediterranean kumene kuli Israyeli, mvula yoyambilira (cha m’mwezi wa Okutobala) inakonzekeretsa nthaka kuti idzalidwe. Mvula yachiwiri, yotchedwa “masika” (cha m’mwezi wa Epulo), inapatsa nthaka kuthekera kothandizira zakumunda kuti ziche.

Monga momwe Mpingo unayambira ndi mvula ya Mzimu Woyeria, kulalikidwa kwa Uthenga Wabwino komaliza, kukolola kotsiriza, kudzachitika ikadzatsanulidwa mvula ya masika: Mzimu Woyeria udzatsanulidwa mwa mphamvu pa okhulupirira a m’badwo wotsiriza. (Chivumbulutso 18 :1).





KULALIKIDWA KWA UTHENGA WABWINO

“Zitatha izi ndinaona mngelo wina wakutsika m’Mwamba wakukhala nao ulamuliro waukulu; ndipo dziko linaunikidwa ndi ulemerero wake.” (Chivumbulutso 18:1)

Yohane anaona “mngelo wina” akutsika ndi mphamu. Ulemerero wa mngelo ameneyu ukudzaza dziko lonse lapansi (Chivumbulutso 18:1). Kodi mngeloyu akulengeza uthenga wotani?

Uthenga wake ndiwofanana ndi uthenga wa mngelo wachiwiri wakuti: Babulo wagwa ndipo wadetsa mitundu yonse (Chivumbulutso 18:2-3; 14:8).

Mzimu Woyeria adzatsikira mwa mphamu pa okhulupirika “iwo akusunga malamulo a Mulungu, ndi chikhulupiriro cha Yesu” (Chivumbulutso 14:12), ndi omwe akulalikira kale Uthenga Wabwino, pamodzi ndi chenjezo la chiyambi cha chiweruzo, ndi kuitanira anthu kulambira Mlengi.(Chivumbulutso 14:6-7).

Poyang’anzana ndi mauthenga amenewa, komanso chifukwa cha mphamu ya mvula ya masika, anthu adzayangánizana ndi kusankha chimodzi mwa zothekera ziwiri: kuvomereza chisindikizo cha Mulungu kapena chizindikiro cha chilombo.(Chivumbulutso 14:9-11).

Mawu ambiri adzalalika uthenga womaliza. Ambiri adzasankha kukhala okhulupirika mpaka mapeto.



**“Kutsika kwa Mzimu Woyerpa mpingo kukuyembekezereka kukhala
chochitika cha mtsogolo, koma ndi mwayi wapadera wa mpingo
kulandila iwo tsopano. Funani, pempherereni, ndipo khulupirirani Iwo.
Tiyenera kukhala nawo, ndipo Kumwamba kuli kokonzeka kutipatsa.”**

EGW (Last Days Events, pg. 189)

**“Koma palibe m'modzi amene akuyenera kuzunzidwa ndi mkwiyo wa
Mulungu kufikira chowonadi chitalowa m'maganizo mwake ndi
m'chikumbumtima chake, koma kukanidwa. Alipo ambiri amene
sanakhalepo ndi mwayi wakumva choonadi chapadera mu nthawi ino.
Kufunikira kwa lamulo lachinayi sikunayikidwepo pamaso pawo
m'kuunkika kwake kwenikweni. Iye amene amawerenga za mu mtima
uliwonse, ndikuyesa zolina zonse, sadzasiya aliyense wofuna
kudziwa choonadi, kuti anyengedwe pa nkhani ya mkangano.
Lamuloli siliyenera kuumirizidwa kwa anthu muchimbulimbuli.
Aliyense ayenera kukhala ndi kuwala kokwanira kuti apange
chisankho chake mwanzero.”**

EGW (The Great Controversy, pg. 605)